-Yesu anabwera pa dziko la pansi lino kudzatichiza ife ku tchimo.
-Yesu anabwera pa dziko la pansi lino kudzatichiza ife ku imfa.
-Yesu anabwera pa dziko la pansi lino kudzatichiza ife kwa Satana.

-Palibe munthu wina aliyense amene angathe kutichiza ife; Yesu yekha ndi amene engathe kutichiza ife.



## PHUNZIRO 50

1. Kodi chifukwa chiyani Satana anamuyesa Yesu?
-Chifukwa chakuti Satana ankafuna kuti Yesu achimwe.

2. Kodi chifukwa chiyani Satana ankafuna kuti Yesu achimwe?
-Chifukwa chakuti Satana sankafuna kuti Yesu aŵapulumutse anthu.

3. Kodi Yesu anakatha kutembenuza miyala kukhala mkate?
-Inde.
-Yesu anali Mulungu.
-Yesu anakatha kuchita china chilichose.

4. Kodi Yesu anamuyankha chiyani Satana?
-Yesu anamuwuza Satana kuti kukhulupilira Mawu a Mulungu ndi kofunika kwambiri kuposa zakudya.

5. Ngakhale kuti Yesu anali ndi njala, kodi nanga chifukwa chiyani Yesu sanatembenuze miyala kuti ikhale mkate?
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate sanamuwuze Iye kuti apange zimenezo.
-Yesu sanamumvere Satana.
-Yesu anamumvera Mulungu Atate.

6. Kodi Satana ankazidziŵa zimene zinalembedwa M’buku la Mulungu , Bayibulo?
-Inde.
-Satana akuzidziŵa zimene zalembedwa M’buku la Mulungu, Bayibulo.

7. Kodi Satana amachita chiyani ndi mawu a Mulungu?
-Satana amaŵasemphanitsa mawu a Mulungu kuti aŵatchere anthu.

8. Kodi chifukwa chiyani kunali kotheka kuti Satana amupatse Yesu zonse za pa dziko la pansi?
-Chifukwa chakuti Adamu atamumvera Satana, iye anasanduka kukhala mbuye wa Adamuyo pamodzi ndi anthu onse a pa dziko la pansi.

9. Kodi Yesu anamupambana bwanji Satana?
-Ndi mawu a Mulungu.

10. Kodi Yesu anaŵasemphanitsa mawu a Mulungu?
-Iyayi.
-Yesu analankhula mawu a Mulungu ngati m'mene analembedwera M'buku la Mulungu, Bayibulo.

11. Kodi Yesu ndi Satana wamkulu ndani?
-Yesu.

12. Kodi chifukwa chiyani Yesu ndi wamkulu kuposa Satana?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Pachiyambi, anali Yesu amene anamulenga Lusifala ngati m'ngero wolungama kwambiri.

13. Kodi Yesu adzachita chiyani kwa Satana ndi ziwanda zache zonse mtsogolo muno?
-Mtsogolomo, Yesu adzamuponya Satana ndi ziwanda zache zonse mu Nyanja ya Moto Wosatha.

-Yohane M'batizi ankapitilizabe kuŵawuza Ayuda kuti atembenuke mitima yawo.

-Tsiku lina mfumu yoyipa kwambiri dzina lache Herodi, anamuyika Yohane M'batizi m'ndende.

-Pamene Yohane M'batizi anayikidwa m'ndende, Yesu



-Kodi nanga chifukwa chiyani munthuyo anapita kwa Yesu?
-Chifukwa chakuti anadziŵa kuti Yesu yekha ndi amene anakatha kumuchiza iye.

-Kodi Yesu anamuchiza iye?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:41-42

41-Ndi chifundo, Yesu anatambasula dzanja lache ndi kumukhudza munthuyo akuti, 'Ine ndikufuna, yeretsedwa!"
42-Nthaŵi yomweyo khatelo linamusiya ndipo anachiritsidwa.

-Yesu anamukhuza munthuyo, ndipo anati, "Yeretsedwa, "ndipo munthuyo anachizidwa.

-Yesu yekha, amene ali Mulungu ndi amene anakatha kumuchiza munthuyo.

-Khate lili ngati tchimo.

-Anthu onse sangathe kudzichiza okha ku tchimo ngati m'mene analephelera munthu wa khate uja kudzichiza yekha ku khate.

-Palibe munthu wina aliyense amene angathe kutichiza ife ku tchimo ngati m'mene kunalibile munthu wina aliyense wakuti angathe kumuchiza munthu wa khate uja ku khate lache lija.

-Yesu yekha ndi amene angathe kutichiza ife ku tchimo ngati m'mene anathera kumuchiza munthu wa khate uja ku khate lache lija.

-Yesu ankafuna kuti aŵamasule anthu ku ukapolo wa Satana ndi ziwanda zache.

-Tsiku lina, munthu wa khate anapita kukamuwona Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:40

40-Munthu wina wache wa khate anadza kwa Yesu, namgwadira, namupempha Iye kuti, "Ngati mukufuna, mukhoza kundiyeretsa."

-Kodi khate mumalidziŵa?
-Khate ndi nthenda yoyipa kwambiri imene imadya mnofu ndi khungu la munthu.

-Mu nthaŵi ya Yesu, kunalibe mankhwala a nthenda ya khate.
-Munakakhala ndi khate, simunakachizidwa mu nthaŵi imeneyo.
-Munakakhala ndi khate sibwenzi mutathandizidwa mu nthaŵi imeneyo.

-Kodi munthuyo anakatha kuzichiza yekha ku khatelo?
-Iyayi.
-Kunalibe mankhwala.

-Kodi panali munthu wina aliyense amene anakatha kumuchiza munthuyo?
-Iyayi.
-Kunalibe mankhwala.

-Kodi asing'anga anakatha kumuchiza munthuyo?
-Iyayi.
-Kunalibe mankhwala.



anayamba kuŵaphunzitsa Ayuda.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:14

14.Yohane M'batizi uja atamuyika m'ndende, Yesu anafika ku Galileya ndi kumalalikira Nkhani Zabwino za Mlungu.

-Yasu anayamba kuŵaphunzitsa Ayuda ali ndi zaka 30.

-Yesu anaŵaphunzitsa Ayuda Nkhani Zabwino za Mulungu.

-Kodi Nkhani Zabwino za Mulungu ndi zotani?
-Nkhani Zabwino za Mulungu zinali zakuti ngakhale kuti machimo onse a anthu ayenera kulandira chilango cha imfa yosatha, Mulungu ankatumiza Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu onsewo

-Kodi Mpulumutsi amene anamutumiza Mulungu kudzaŵapulumutsa anthu anali ndani?
-Yesu.

-Kodi china ndi chiyani chimene ankaphunzitsa Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:15

15-Ankati kuti, "Nthaŵi yofunika yakwana, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira. Tembenukani mitima ndipo mukhulupilire Nkhani Zabwino za Mulungu."

-Kodi Yesu ankatanthawuza kuti chiyani pamene analankhula kuti, "Ndaŵi yakwana ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira?"
-Yesu ankatanthawuza kuti nthaŵi yakwana yakuti Ufumu wa Mulungu ugonjetse ufumu wa Satana ndipo

Mpulumutsi adzamugonjetsa Satana.

-Yesu anaphunzitsanso kuti anthu ayenera kukhulupilira M'mawu a Mulungu.

-Kodi ndi njira yanji imene munthu angathe kumusan-galatsa nayo Mulungu?
-Pokhulupilira M'mawu a Mulungu.

-Pamene Yesu anayamba kuŵaphunzitsa Ayuda, anaŵayitana anthu ena kuti adzikhala ndi Iye.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:16-20

16-Ndipo pamene Yesu ankayenda mphepete mwa nyanja ya Galileya, anamuwona Simoni pamodzi ndi Andi-leya, m'bale wache, akuponya khoka m'nyanjamo pakuti anali asodzi.
17-Yesu analankhula kuti, Nditsateni Ine, ndipo Ine ndidzakupangani inu kukhala asodzi a anthu."
18-Ndaŵi yomweyo anasiya khoka lawolo ndikumut-sata Iye.
19-Ndipo anayenda kupita patsogolo pang'ono, ana-muwona Yakobo, mwana wa Zebedayo, ndi Yohane m'bale wache, nawonso anali m'chombo akukonza ma-koka awo.
20-Ndipo nthaŵi yomweyo anaŵayitana:ndipo anaŵasiya atate awo, Zebedeyo, m'chombo momwemo pamodzi ndi a ntchito olembedwa ndikumutsata Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anaŵayitana anthu ena kuti adzikhala ndi Iye?
-Chifukwa chakuti ankafuna kuti aŵaphunzitse iwowo ndi cholinga chakuti nawonso adzaŵaphunzitse anthu ena Mawu a Mulungu.



34-Ndipo anachiritsa anthu ambiri odwala nthenda za zitundu yosiyanasiyana. Anayiturutsanso mizimu yonyansa yambiri, koma sanayilole kuti yilankhule chifu-kwa chakuti yinkamudziŵa Iye.

-Madzulo amenewo, anthu ankabweretsa odwala ndi og-widwa ndi ziwanda kwa Yesu ndipo Yesu anaŵachiritsa.

-Ichi chinali chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Ichi ndi chifukwa chakuti Yesu akhoza kuchita china chili-chonse.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anaŵachiritsa odwala onse?
-Chifukwa chakuti Yesu ankaŵakonda iwowo.
-Chifukwa chakuti Yesu anali okwiya ndi kudwala kwawo.

-Pachiyambi, Mulungu atalenga dziko la pansi, kanalibe matenda.

-Koma Adamu ndi Hava anamuchimwira Mulungu, ndipo tchimo lawo linabweretsa matenda kwa anthu onse.

-Yesu anafuna kuti achize nthenda imene inabwera ndi tchimo pa dziko la pansi pano.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anaŵachiritsa anthu onse amene anagwidwa ndi ziwanda?
-Chifukwa chakuti Yesu ankaŵakonda iwowo.
-Chifukwa chakuti Yesu anali okwiya chifukwa chakuti zi-wanda zinkaŵapangitsa anthu kukhala akapolo.

-Pachiyambi, anthu anali ana a Mulungu.

-Koma Adamu ndi Hava atamuchimwira Mulungu, anthu onse anasanduka kukhala akapolo a Satana ndi ziwanda.

-Yesu anachilamula chiwandacho kuti chikhale chete ndipo chituruke mwa munthuyo.

-Kodi chiwandacho chinamumvera Yesu?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani chiwandacho chinamumvera Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu ali ndi mphamvu kwambiri kuposa ziwanda.

-Kodi anthu anaganiza chiyani atamuwona Yesu akumupulumutsa munthu ku chiwanda?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:27-28

27-Ndipo anthu onse anazizwa kwambiri, kotero kuti anafunsana kuti, “Ichi mchiyani? Chiphunzitso chatsopano ndi mphamvu! Alamula ngakhale mizimu yonyansa ndipo ikumumvera Iye.”
28-Ndipo mbiri ya Iye inafala mofurumira ponseponse mu dziko lonse lozungulira Galileya.

-Anthu anazizwa kwambiri atamuwona Yesu akumupulumutsa munthu ku chiwanda.
-Anthu anazizwa kwambiri atachiwona chiwanda chikumumvera Yesu.

-Kodi kenako madzulo chinachitika ndi chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:32-34

32-Ndipo madzulo, dzuŵa litaloŵa, anadza nawo kwa Iye onse odwala ndi ogwidwa ndi mizimu yonyansa.
33-Ndipo mudzi onse unasonkhana pa khomo.



-Kodi ntchito ya anthu ena amene anayitanidwa ndi Yesu kuti adzikhala naye inali yotani?
-Ena anali asodzi a a msomba.

-Tsiku lina lache Yesu anapita mu mzinda wotchedwa Kapenamu kukaŵaphunzitsa Ayuda.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:21

21-Kenako Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anapita ku Kapenamu. Pa tsiku la sabata, Yesu analoŵa mu sunagogi, ndipo anayamba kuphunzitsa.

-Pamene Yesu anafika mu mzinda wa Kapenamu, anapita mu sunagogi kukaphunzitsa.

-Kodi sunagogi inali chiyani?
-Sunagogi inali nyumba imene Ayuda ankakumanilanamo ndikumaŵerenga Mawu a Mulungu, Bayibulo.

-Kodi Ayuda ambiri ankaganiza chiyani za chiphunzitso cha Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:22

22-Anthu anazizwa kwambiri ndi chiphunzitso chake, chifukwa chakuti anaŵaphunzitsa monga mwini mphamvu, osakhala ngati aphunzitsi a malamulo.

-Ayuda ambiri anazizwa ndi chiphunzitso chaYesu.

-Kodi chifukwa chiyani Ayuda ambiri anazizwa ndi chiphunzitso cha Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu anaŵaphunzitsa iwo mwa mphamvu ndi mzeru.

-Kodi aphunzitsi a malamulo anali ndani?
-Anali Afarisi.

-Kodi chiphunzitso cha Yesu ndi Afarisi chinkasiyana bwanji?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu, ankamudziŵa Mulungu Atate.
-Afarisi sankamudziŵa Mulungu Atate.

-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu, Iye ankaŵadziŵa bwino Mawu a Mulungu
-Afarisi sankaŵadziŵa bwino Mawu a Mulungu.

-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu, Yesu ankakhulupilira mu liwu lililonse la Mulungu.
-Afarisi sankaŵakhulupilira Mawu a Mulungu.

-Pamene Yesu ankaphunzitsa, munthu wogwidwa ndi mizimu yonyansa anakuwa.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:23-24

23-Ndipo munthu amene anali ndi mzimu wonyansa mu sunagogi mwawomo, anafuwula kwambiri kuti,
24-"Kodi ukufuna chiyani ndi ife, Yesu wa ku Nazareni? Kodi wabwera kudzatiwononga ife? Ndikukudziŵa kuti iwe -- ndi Woyerayo wa Mulungu!"

-Pachiyambi, kodi ziwanda zinali chiyani zisanakhale ziwanda?
-Pachiyambi, ziwanda zinali angelo abwino amene analengedwa ndi Mulungu mpaka pamene anamutsata Satana ndikusanduka kukhala oyipa.

-Ziwanda zimakonda kukhala mwa anthu amene sakhulupilila Mulungu.



-Chiwanda chinkakhala mwa munthu amene anafuwulayo.

-Kodi chiwandacho chinadziŵa kuti amene ankaphunzitsayo anali Yesu?
-Inde.

-Kodi chiwandacho chinadziŵa kuti Yesu anali Mulungu?
-Inde.

-Kodi chiwandacho chinadziŵa kuti Yesu anali olungamika, oyera ndiponso amadana ndi machimo onse?
-Inde.

-Kodi chiwandacho chinadziŵa kuti Yesu anali ndi mphamvu kwambiri kuposa ichocho?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani chiwandacho chinkamuwopa yesu?
-Chifukwa chakuti chinkadziŵa kuti Yesu anali ndi mphamvu yochitumiza ichocho ku Nyanja ya Moto Wosatha nthaŵi iliyonse.

-Chiwanda chinkadziŵa kuti Yesu anali ndi mphamvu yochitumiza ku Nyanja ya Moto Wosatha pa nthaŵi imeneyo.

-Kodi Yesu anayankha chiyani kwa chiwandacho?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 1:25-26

25-"Ndipo Yesu anawudzudzula kuti, "Khala chete ndipo utuluke mwa iye!"
26-Ndipo mzimu wonyansawo unamunjenjemeletsa kwambiri ndi kufuwula ndi mawu akuru munthu uja kenako ndikuturuka mwa iye.